## PHUNZIRO LA 42

1-Ngakhale kuti zaka zambiri zinapita Mulungu chilonjezereni zotumiza Mpulumutsi, kodi Mulungu analiyiŵala lonjezo lache?
-Iyayi, Mulungu sanaliŵalile lonjezo lache.

2-Kodi Mulungu anapereka mawu ache kwa ndani onena za Mpulumutsi amene ankabwerayo?
-Aneneri.

3-Kodi mawu amene Mulungu anapereka kwa Aneneri analembedwa pati okamba za Mpulumutsi amene ankabwerayoŵ?
-M'buku la Mulungu, Bayibulo.

4-Kodi a Isirayeli ambiri anaŵamvera Aneneri a Mulungu?
-Iyayi.

5-Kodi a Isirayeli anachita chiyani kwa Aneneri a Mulungu?
-Ankaŵapha Aneneriwo.

6-Kodi a Isirayeli ankaŵamvera ndani m'malo moŵamvera Aneneri a Mulungu?
-Aneneri abodza.

7-Aneneri abodza ankanena kuti iwowo ankanena zowona za Mulungu, koma kodi kwenikweni ankanena za chiyani?
-Za bodza la Satana.

8-Kodi masiku ano, Satana akupitirizabe kulankhula za bodza zache kudzera mwa anthu?
-Inde.

9-Ngakhale kuti a Isirayeli ankazipembedza zosema zimene iwo anazipanga, kodi iwowo ankapitirizabe ku-

mamupembedza Mulungu Mnyumba yache?
-Inde.

10-Kodi Mulungu ankakulandira kupembedza kwa a Isirayeli amene ankapembedza zosema zimene iwowo ankazipanga, ndikumamupembedzanso Mulungu Mnyumba yache?
-Iyayi.

11-Kodi chifukwa chiyani?
-Chifukwa chakuti Mulungu ankadziŵa kuti iwowo ankamupembedza Iye ndi milomo yawo yokha.
-Chifukwa chakuti Mulungu ankadziŵa kuti iwowo ankazipembedza zosema m'mitima mwawo.

12-Kodi ndani amene amazidziŵa zonse za m'mitima mwathu?
-Mulungu.

13-Kodi Mulungu amalankhula chiyani za mitima yathu yonse?
-Amalankhula kuti mitima yathu yonse yadzadza ndi machimo.

14-Ngakhale kuti a Isirayeli ankazipembedza zosema, kodi panali a Isirayeli ena amene ankamupembedza Mulungu yekha?
-Analipo ochepa.

15-Kodi a Isirayeli amene ankamupembedza Mulungu yekha, ankamuyembekezera ndani?
-Ankamuyembekezera Mulungu kuti atumiza Mpulumutsi.

-Mulungu ndi ofatsa.

-Mulungu akuŵayembekezera anthu kuti atembenuke kuchokera



iwowo ankakhulupilira kuti analibe machimo.

-Kodi kungokhala ndi ndalama zambiri kokha kungakupangitseni inu kukhala opanda machimo?
Iyayi.

-Asaduki ambiri sankamukhulupilira Mulungu.

-Mu nthaŵi zimenezi, Ayuda anamanga nyumba zokumanilanamo.

-Nyumba zimene ankakumanilanamo Ayuda zinkatchedwa kuti ma sunagogi.

-M'masunagogi, Ayuda ankakumanamo ndi kumaŵerenga ndiponso kukambirana zimene Mose analemba.

-Ayuda anamanga ma Sunagogi m'mizinda yawo yonse.

-Pa tsiku lomaliza la pa mulungu, Ayuda ankapita M'masunagogi mwawo ndikumakamvera zimene analemba Mose.

-Nthaŵi zambiri anthu ankalongosola za zolembedwa ndi Mose.

-Koma chifukwa chakuti anthu sankamukhulupilira Mulungu, kulongosola kwawo pa zimene Mose analemba, kunali kolakwika.

-Ngakhale kuti Ayuda ambiri sankamukhulupilira Mulungu, panali ayuda ena pang'ono amene ankamukhulupilira Mulungu.

-Ayuda ameneŵa ankamuyembekezera Mulungu kuti atumiza Mpulumutsi.

-Afarisi ankakhulupilira kuti iwowo ankaŵamvera mal-amulo onse a Mulungu.

-Kodi pali amene angathe kumvera malamulo onse a Mulungu?
-Palibe.

-Chifukwa chakuti Afarisi ndi amene ankaphunzitsa mawu a Mulungu, iwowo anali odzikonda.
-Chifukwa chakuti Afarisi ndi amene ankaphunzitsa mawu a Mulungu, iwowo ankakhulupilira kuti ankaŵadziŵa kwambiri mawu a Mulunguwo.

-Kodi kungophunzitsa kokha kwa mawu a Mulungu kungakupangitseni inu kuŵamvetsa mawu a Mulunguwo?
-Iyayi.

-Chifukwa chakuti Afarisi ndi amene ankaphunzitsa mawu a Mulungu, iwowo ankakhulupilira kuti alibe machimo.

-Kodi kungophunzitsa mawu a Mulungu kokha kungakupangitseni inu kukhala opanda machimo?
Iyayi.

-Afarisi ambiri sankamukhulupilira Mulungu.

-Atsogoleri ena a Ayuda ankatchedwa kuti Asaduki.

-Asaduki anali olemera ndiponso anali a ndalama zambiri.
-Asaduki ankayang'aniranso ku Nyumba ya Ambuye.

-Chifukwa chakuti Asaduki anali olemera kwambiri ndipon-so ankayang'anira ku Nyumba ya Mulungu, iwowo anali odzikonda.
-Chifukwa chakuti Asaduki anali ndi ndalama zambiri,



chokera ku njira zawo zoyipa ndikumatsata njira yache.

-Mulungu anayembekezera kwa zaka 120 kuti anthu a mu nthaŵi ya Nowa atembenuke kuchokera ku njira zawo zoyipa kuti atsate njira ya Mulungu.

-Mulungu anayembekezeranso kwa zaka zokwana 200 kuti a Isirayeli asiye njira zawo zoyipa kuti atsate njira ya Mulungu.

-Koma a Isirayeli sanamukhulupilire Mulungu.
-A Isirayeli ankaganiza kuti Mulungu ayiwala machimo awo.

-Kodi Mulungu anaŵayiwala machimo awo?
-Iyayi.

-A Isirayeli ankaganiza kuti Mulungu sapereka chilango pa machimo awo.

-Kodi Mulungu anapereka chilango pa machimo awo?
-Inde.

-Mulungu anapereka chilango kwa a Isirayeli ngati m'mene anaperekera chilango pa machimo a anthu a m'masiku a Nowa.

-Kodi Mulungu anapereka chilango chotani kwa mitundu khumi ya ku Isirayeli?
-Mulungu anaŵatumiza Asiliya kukayiputa mitundu khumi ya ku Isirayeli ndikuŵapanga iwowo ngati akapolo awo.

Tiyeni tiŵerenge 2 Mafumu 17:5-8

5-Mfumu ya ku Siliya anagumula ndikulizungulira dzikolo, anayenda kukalimbana ndi a Samaliya ndipo analizungulira kwa zaka zitatu,

6-Mchaka cha chisano ndi zinayi chimene ankalamulira Hosheya, ufumu wa a Siliya unalanda dziko la Samaliya. Ndipo anaŵatenga a Isirayeli kukhala akayidi awo, ndipo ena mwa iwowo anaŵakhazika mu mzinda wa Halani, ena poŵandikana ndi mtsinje wa Habulo mu mzinda wa Gosani, ena m'mizinda ya Mediya.

7-Samaliya inagwa chifukwa chakuti a Isirayeli anaŵalakwira Ambuye, Mulungu wawo, amene anaŵapulumutsa iwowo kwa mfumu wa ku Iguputo ndikuŵatsogolera poturuka mu Iguputo. Ndipo iwowo ankayipembedza milungu ina,

8-ndikumatsata khalidwe la anthu amene anathamangitsidwa ndi Ambuye, ndipo atengera khalidwe la mafumu a ku Isirayeli.

-Asiliya anayiyamba mitundu khumi ya ku Isirayeli, ndipo anaŵatenga iwowo ndikupita nawo ku Siliya kukuŵapanga iwowo kukhala akapolo awo.

-Asiliya anafikanso ndi anthu ochokera ku mayiko ena kuti adzikhala ndi a Isirayeli amene anatsalira ku dziko la Isirayeli.

-Anthu ochokera ku mayiko ena amene anafika nawowo, sankamukhulupilira Mulungu koma ankangozipembedza zosema zimene iwowo anazipanga.

-Anthu ameneŵa ankakwatirana ndi a Isirayeli amene anatsalira mu dziko la Isirayeli ndipo mtundu watsopano unayambika.

-Mtundu wa anthu atsopanowo umkatchedwa kuti Asamaliya.



-Chifukwa chakuti anthu ambiri ankafuna kuti adziŵerenga mawu a Mulungu, kunali kofunika kwambiri kulemba mawu a Mulungu pa zidutswa zatsopano za mapepala.

-Masiku onse, Alembi ankalemba pa zidutswa zatsopano za mapepala mawu a Mulungu omwewo amene anali pa mapepala akale.

-Chifukwa chakuti Alembi ndi amene ankalemba mawu a Mulungu, iwowo anali odzikonda.
-Chifukwa chakuti Alembi ndi amene ankalemba mawu a Mulungu, iwowo ankakhulupilira kuti ankaŵadziŵa kwambiri mawu a Mulunguwo.

-Kodi kungolemba mawu a Mulungu kokha kungakupangitseni inu kuŵamvetsa mawu a Mulunguwo?
-Iyayi.

-Chifukwa chakuti Alembi ndi amene ankalemba mawu a Mulungu, iwowo ankakhulupilira kuti alibe machimo.

-Kodi kungolemba mawu a Mulungu kokha kungakupangitseni inu kukhala opanda machimo?
Iyayi.

-Alembi ambiri sankamukhulupilira Mulungu.

-Atsogoleri ena a Ayuda ankatchedwa kuti Afarisi.

-Afarisi ankaphunzitsa mawu a Mulungu kwa Ayuda.
-Afarisi ankaphunzitsanso malamulo a Mulungu kwa Ayuda.

-Kuphatikiza apa, Afarisi anapanganso malamulo awo awo amene ankaphunzitsanso kwa Ayuda.

-Pambuyo pa Agiliki, Mulungu anaŵatumiza Aloma kukaŵayamba Ayuda.

-Aloma anaŵagonjetsanso Ayuda ndipo anaŵalandanso dziko lawo.
-Aloma anaŵalamula Ayuda kuti adzipereka nsonkho.
-Aloma anaŵapha Ayuda ambiri ndi mipaliro ndi ma uta.

-Aloma anakhomera pa mtanda Ayuda ambiri.

-Dzina la mfumu wa Aloma linali Kayisala.
-Kayisala ankakhala mu mzinda wa Loma.
-Aloma ankazipembedza zosema zambiri.
-Aloma nawonso ankamupembedza mfumu yawo, kayisala.

-Pa nthaŵi imene Ayuda ankakhala mu mzinda wa Yelusalemu, atsogoleri a Chiyuda anali m'maguru atatu.

-Anali Alembi, Afalisi ndi Asaduki.

-Atsogoleri ena a Ayuda ankatchedwa kuti Alembi.

-Kale kunalibe mabuku ngati amene tilinawo masiku ano.

-Anthu akafuna kulemba china chake, ankalemba pa chidutswa chachitali cha pepala chimene ankachipinda mbali zonse.

-Mose analemba mawu a Mulungu pa zidutswa zazitali za mapepala zimene ankazipinda mbali zonse.

-Aneneri ena nawonso analemba mawu a Mulungu pa zidutswa zazitali za mapepala zimene ankazipinda mbali zonse.



-Asamaliya ankamupembedza Mulungu mu njira yawo.

-Pamene Mulungu anamaliza kupereka chilango kwa mitundu khumi ya ku Isirayeli ija, kodi Mulungu anayipatsa chilango chotani mitundu yiŵiri ya ku Yuda ija?
-Mulungu anatumiza anthu a ku Babeloni kuti akayiyambe mitundu yiŵiri ya ku Yuda, ndikuŵapanga iwowo kukhala akapolo awo.

Tiyeni tiŵerenge 2 Mafumu 25:1-7

1-Chomcho mu chaka cha chisano ndi zinayi chimene ankalamulira Zadekiya, pa tsiku la khumi la mwezi wa khumi, Nebukadineza, mfumu ya ku Babeloni anapita ku Yelusalemu ndi asilikali ache a nkhondo ndipo anathira nkhondo. Anamanga masakasa pamodzi ndi linga lozungulira masakasawo.
2-Mzinda wa Yelusalemu anawuzinga mpaka mchaka cha 11 chimene ankalamulira mfumu Zadekiya.
3-Pa tsiku la chisano ndi anayi a mwezi wa chinayi mu chaka chomwecho, njala inakula kwambiri mwakuti anthu analibe chakudya.
4-Ndipo linga la mzindawo linagumulidwa, ngakhale kuti a Babeloni anali atawuzungulira mzindawo, asilikali onse anathaŵa pakati pa usikuwo. Anathaŵa podzera m'njira ya ku munda wopatulika wa mfumu ndipo anapita kukadutsira pa chipata chimene chimkalumikiza makhoma aŵiri, kenako anathaŵira ku Araba.
5-Koma asilikali a ku Babeloni anamutsatira mfumu Zedekiya, anamugwilira m'chigwa cha Yeriko ndipo asilikali ache onse anamusiya ndikumwazikana.
6-Zedekiya anamutengera kwa mfumu ya ku Babeloni amene anali mu mzinda wa Libila, ndipo kumeneko Nebukadineza analamulira kuti Zadekiya aphedwe.

7-Anaŵaphanso ana ache a Zedekiya mwini wache akuyang'ana. Kenako anaŵakolowola maso a Zedekiya ndipo anamumanga ndi unyolo ndikumutengera ku Babeloni.

-Anthu a ku Babeloni anayiyamba mitundu yiŵiri ya ku Yuda, ndi kuŵatenga iwowo kupita nawo ku Babeloni kukakhala akapolo awo.

-Anthu a ku Babeloni anawuwononganso mzinda wa Yelusalemu.

Tiyeni tiŵerenge 2 Mafumu 25:9-12 ndi 21

9-A Babeloni anawotcha Nyumba ya Mulungu Ambuye, nyumba ya mfumu ndi nyumba zina za anthu odziŵika mu Yelusalemu.
10-Ndipo asilikali anagwetsa malinga a mzinda wa Yelusalemu.
11-Kenako Nebuzaladani anaŵatengera ku Babeloni anthu onse amene anatsalira mu mzindawo, pamodzi ndi onse ogwira ntchito zofunika, anaŵatengera kwa mfumu ya ku Babeloni.
12-Koma anthu ena amene anali ovutika kwambiri, amene analibe china chilichonse, anaŵasiya ku Yuda, ndipo anaŵapatsa tchito yolimira mitengo ndi ku minda.
21-Chomcho anthu a ku Yuda anapita ku ukapolo, kotalikirana ndi dziko lawo.

-Kodi anthu a ku Babeloni anawuwononga bwanji mzinda wa Yelusalemu?
-Anayiwotcha ndi moto Nyumba ya Mulungu.
-Anayiwotcha Yelusalemu yonse.
-Anagwetsa linga lozungulira mzinda wa Yelusalemu.

-Mulungu anapereka chilango kwa mitundu khumi ya ku



Isirayeli ndi mitundu iŵiri ya kuYuda chifukwa chakuti sanazisiye njira zawo za machimo.

-Patapita zaka zambiri anthu a ku Yuda amene ankakhala ku Babeloni, analilira kwa Mulungu.

-Iwowo analilira kwa Mulungu, kuvomereza machimo awo kwa iye, ndikumupemphe Iye kuti aŵakhululukire.

-Chifukwa chakuti Mulungu ndi wachisoni, anaŵalora ambiri mwa iwo kuti abwerere ku mzinda wa Yelusalemu.

-Kodi anthu a ku Yuda anachita chiyani atabweleranso ku Yelusalemu?
-Anamanganso Nyumba ya Mulungu.
-Anawumanganso mzinda wa Yelusalemu.
-Anamanganso linga lozungulira mzinda wa Yelusalemu.

-Anthu a ku Yuda amene anabwelera ku Yelusalemu amkatchedwa ndi dzina latsopano.

-Dzina latsopano la anthu a ku Yuda linali Ayuda.

-Ngakhale kuti Ayuda ankamupembedza Mulungu, iwowo anapitirizabe kumazipembedzanso zosema zimene anazipanga.

-Chomcho Mulungu anaŵatumiza anthu a mitundu iŵiri kudzaŵayamba iwowo.

-Poyamba Mulungu anaŵatumiza Agiliki kukaŵayamba Ayuda.

-Agiliki anaŵagonjetsa Ayuda ndikuŵalanda dziko lawo.
-Agiliki ankaŵaphunzitsanso Ayuda kulankhula chilankhulo chawo cha Chigiliki.